

Khadi Lapafupi la Ciwerengero ca Umphawi Zambia Simple Poverty Scorecard® Poverty-Assessment Tool

18 Juni 2017

Ili ibula lile sangwa mu Cibemba pa SimplePovertyScorecard.com

This document is available in English at SimplePovertyScorecard.com.

Chikalata ici cipezeka mu Chinyanja pa kangaude wa SimplePovertyScorecard.com

Chifupikitso

Khadi Lapafupi la Ciwerengero ca Umphawi igwiritsa nchito zizindikiro khumi za mtengo wotsika za mu dziko la Zambia, kucokera mu Kafukufuku wocitika mu 2015 wochedwa Living Conditions Monitoring Survey woona pa zofunikira za panyumba pofuna kuona m'mene anthu akukwaniritsira umoyo wa tsiku ndi tsiku. Ocita nchito ya kafukufuku imeneyi atha kutenga mayankho ofunikira mwa mphindi khumi cabe. Zotuluka mu khadi la ciwerengero imeneyi zithandiza kudziwa za umphawi wa anthu m'dziko. Khadi la ciwerengero imeneyi imathandizira kuona ndi kuika m'malo ndondomeko zoyenera pakuthana ndi umphawi pakati pa anthu komanso kuona m'mene ndondomeko zimene zilipo kale zikuthandizira pa kucepetsa umphawi mu Zambia (monga momwe mudzaonera mu zolembeka), komanso kuitanitsa cithandizo.

Ganizo limeneli

Dziko la Zambia linasintha tanthauzo la liu lace la *umphawi* pakati pa caka ca 2010 ndi 2015. Pepala ili likonza cipangizo ca khadi la ciwerengero mu Schreiner (2013a) poona pa tanthauzo latsopano la umphawi mogwiritsa nchito mfundo za mu 2015. Kucokera tsopano onse ogwiritsa nchito zimenezi akhoza kuyerekeza kusintha kwa tanthauzo la tsopano imene ili pano komanso atha kuona ngakhale tanthauzo lakale mu Schreiner (2013a). Koma ziyerekezo za kusintha zomwe ziima pa mfundo za kafukufuku wocitika m'zaka za kumbuyo kwa 2015, siziri zolondoloka bwino. Motero, ziyerekezo za kusintha pa umphawi wodza ndi kusowekera kwa cakudya ayenera kugwiritsa nchito tanthauzo la tsopano pokhapo ngati akugwiritsa nchito mfundo zotuluka kucokera m'caka ca 2015 ndi zaka zotsatapo. Mfundo za m'zaka za kumbuyo kwa 2015 zitha kugwiritsidwa nchito poona pa kasinthidwe ka kagawanidwe ka umphawi pogwiritsa nchito zotulukamo mu khadi la ciwerengero (osati kusintha kwa mlingo wa zothekera za umphawi) la umphawi wa kusowekera katundu (osati umphawi wakusowekera cakudya) pogwiritsa nchito tanthauzo la *umphawi*.

Mayamiko

Mfundo zimenezi zacokera ku ofesi la pakati la ziwerengero la Central Statistical Office. Ciyamiko cipite kwa Alejandro de la Fuente, a Frank Kakungu, ndi a John Kalumbi. Nkhani imeneyi yonse inatembenezidwa kucotsa m'Chingerezi ndi kulembedwa m'Cinyanja ndi Japhet Mphande, japhetmphande@yahoo.com. Pepala limeneli lalembedwa pokumbukira a Muhammad Awais Butt ndi a Martín Cumpa Castro. Copyright © 2017 by Microfinance Risk Management, L.L.C., all rights reserved. "Simple Poverty Scorecard" is a Registered Trademark of Microfinance Risk Management, L.L.C.

Wolemba

Mark Schreiner atsogolera bungwe la Microfinance Risk Management, L.L.C. Iwonso ndi mkulu wa za maphunziro pa Center for Social Development pa Washington University in Saint Louis.

Khadi Lapafupi la Ciwerengero ca Umphawi

Cidziwitso ca mafunso:	_____	Dzina	Wodziwitsa
Tsiku la mafunso:	_____	Wotengako mbali:	_____
Dziko:	ZMB	Woyanganira gawolo:	_____
Khadi la ciwerengero:	001	Malo acithandizo:	_____
Kulemera kwa citsanzo:	_____	Nambala ya onse okhala m'nyumba:	_____

Coonetsera	Yankho	Mapointsi	Score
1. Kodi pa nyumba pali anthu angati?	A. Eyiti kapena ambiri B. Seveni C. Sikisi D. Faifi E. Folo F. Filii G. M'modzi kapena awiri	0 7 9 11 15 21 29	
2. Kodi anthu onse okhala pa nyumbapo a zaka 7 mpaka 16 amapita ku sukulu?	A. Ai B. Inde C. Palibe a 7 mpaka 16	0 3 6	
3. Kodi ndi m'giredi bwanji m'mene mkazi (wamkulu) mutu (wotsogolera)/amwao anapelera sukulu?	A. Palibe ngakhale woyamba kufika mu giredi 1 ngakhale mu giredi 5 B. Giredi 6 C. Giredi 7 mpaka Giredi 9 D. Palibe mkazi wotsogolera E. Giredi 10 ndi kupita pamwamba	0 2 4 5 9	
4. Kodi pansi pa nyumbayo pali bwanji? (Ngati nkotheke onani, musafunse)	A. Thope, mitengo cabe, kapena zina B. Konkiriti cabe, kapena sementi	0 2	
5. Kodi denga (mtenje) la nyumba linamangidwa ndi ciani? (Ngati nkotheke onani, musafunse)	A. Udzu/maphesi, kapena zina B. Malata, kapena zina zosakhala matailosi ya asibesitazi C. Konkiriti, asibesitazi, kapenamatailosi ya asibesitazi	0 3 5	
6. Kodi kwenikweni m'magwiritsa nchito mphamvu yotani pophika panyumba pano?	A. Nkhuni (zotola nokha kapena zogula), malasha a mwala, zomera/matuvi a ziweto kapena zina B. Malasha (odzipangila kapena ogula) C. Gasi, malaiti, sola kapena parafini	0 4 15	
7. Kodi m'nyumba yanu muli ndi wailesi yakanema (TV), ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi/ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV?	A. Mulibe TV (ngakhale zina zilipo) B. TV cabe, mulibe zina C. TV, ndi zina (DVD, dishi ndi zina)	0 6 10	
8. Kodi m'nyumbamo muli ndi nsimbi yosakhala ya malaiti kapena ya malaiti?	A. Mulibe B. Muli yosakhala ya malaiti cabe C. Ya malaiti, kapena zonse, ya malaiti ndi yosakhala ya malaiti	0 4 11	
9. Kodi pa nyumbapo muli ndi ma telefoni?	A. Ai B. Inde	0 6	
10. Kodi m'nyumbamo muli ndi mibedi ingati komanso mamatilesi angati?	A. Mulibe B. Bedi imodzi kapena mibedi yambiri koma mulibe matilesi C. Matilesi imodzi (mosawerengera mibedi ndi ingati) D. Mamatilesi awiri kapena ambiri (mosawerengera mibedi ndi ingati)	0 2 4 7	

Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito:

Maina a Am’Nyumba, Zaka, ndi Maphunziro a Sukulu

Mu mutu wa khadi la ciwerengero, lembani codziwitsira mafunso (ngati ndi codziwika), tsiku la mafunso, ndi kulemera kwa citsanzo ca wotengako mbali (ngati nkotheke). Mukatero, mulembe maina onse, ndi manambala odziwitsa wotengako mbali, komanso ya inu ngati wofunsa, komanso pointi ya cithandizo (sevisi) imene wofunsidwa akugwiritsa nchito.

Woyankhayo sayenera kukhala wotengako mbali mu bungwe lanulo.

Mukatero, muwerenge kwa woyankhayo: *Conde ndipatseni dzina loyamba kapena dzina lopeka ya anthu onse amene nthawi zambiri amakhala ndi inu m’nyumba yanuyi. Muyambe ndi mutu wa banja, kenako alendo omwe akhala kucokera miyezi sikisi akuceza. Mulembenso maina ya mamembala ena amene mwina anapita ukaceza kwina, amene ali ku chipatala, ku masukulu ogona komweko, ku ma koleji, kapena ku yunivesite, ndi malo ena otero. Conde mudiuzenso zaka za wina aliyense. Kwa wina aliyense wa zaka 7 mpaka 16, conde mudiuze ngati ameneyu amapita ku sukulu.*

Mulembe dzina ndi zaka za wina aliyense wokhala m’nyumbamo. Simuyenera kudziwa zaka zenizeni za munthuyo pokhapo zaka zake zoonza zili monga 6 kapena 17. Kucitira patsogolo, muyenera kudziwa ngati mkazi ndiye atsogolera nyumbayo (ngati alipo). Mulembe totala ya mamembala onse pamwamba pa mutu wa khadi la ciwerengero pafupi ndi “Nambala ya onse okhala m’nyumba:”. Mukatero, muchonge yankho ya coonetsera coyamba. Kwa mamembala a zaka za pakati pa 7 kufikira 16, mufunse ngati amapita ku sukulu, ndipo muchonge coonetsera caciwiri. Ngati ndi “Ai” mulembe muzungulira (seko), ndipo muchonge “A. Ai”. Ngati “Siali a zaka 7 mpaka 16” imazunguliridwa pa mamembala onse okhala m’nyumbamo, ndipo muyenera kucongola “C. “Palibe 7 mpaka 16”. Ngati sitero, chongani “B. Inde”.

Muyenera kusungula pamtima matanthauzo onse opezeka mu “Malangizo Olondoledwa Pomasulira Zionetsero za Khadi la Ciwerengero” za zopezeka m’nyumba, membala opezeka m’nyumbamo, ndi kuonetsa za opita ku sukulu.

Dzina loyamba kapena dzina lopeka	Zaka	Ngati <DZINA> ali ndi zaka za pakati pa 7 mpaka 16, kodi iyeyu amapita ku sukulu?
1. (Mutu)		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
2.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
3.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
4.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
5.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
6.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
7.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
8.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
9.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
10.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
11.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
12.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
13.		Siali a zaka 7 mpaka 16 Ai Inde
Nambala ya onse okhala m’nyumba:		—

**Tebulo loonapo posanduliza ziwerengero
kuonetsa kuthekera kwa umphawi:
Tanthauzo latsopano la umphawi wa dziko lonse**

<i>Score</i>	Kuthekera kwa umphawi (%)			
	<u>Umphawi wa m'dziko</u>			
	Cakudya	100%	150%	200%
0-4	95.9	99.8	100.0	100.0
5-9	89.9	97.3	99.9	100.0
10-14	88.0	97.2	99.7	100.0
15-19	82.4	95.1	99.6	100.0
20-24	70.8	86.7	97.6	99.6
25-29	57.2	79.0	93.9	98.4
30-34	46.0	69.2	89.6	96.2
35-39	31.4	55.0	78.4	90.3
40-44	19.7	40.0	69.3	85.3
45-49	6.9	23.6	52.7	76.1
50-54	4.5	16.1	45.2	68.9
55-59	2.8	4.8	25.5	46.9
60-64	1.0	3.2	16.6	33.6
65-69	0.4	2.6	10.2	27.1
70-74	0.1	1.2	6.1	21.7
75-79	0.0	0.2	2.0	9.4
80-84	0.0	0.0	0.0	5.5
85-89	0.0	0.0	0.0	5.4
90-94	0.0	0.0	0.0	0.0
95-100	0.0	0.0	0.0	0.0

**Tebulo loonapo posanduliza ziwerengero
kuonetsa kuthekera kwa umphawi:
Tanthauzo latsopano lokhuza umphawi pakati pa maiko
osiyanasiyana 2005 ndi 2011 umphawi**

<i>Score</i>	Kuthekera kwa umphawi (%)					
	Umphawi PPP 2005				Umphawi PPP 2011	
	\$1.25	\$2.00	\$2.50	\$5.00	\$1.90	\$3.10
0-4	100.0	100.0	100.0	100.0	99.8	100.0
5-9	99.9	100.0	100.0	100.0	98.3	100.0
10-14	99.7	100.0	100.0	100.0	98.3	100.0
15-19	99.1	100.0	100.0	100.0	95.9	99.9
20-24	96.7	99.8	100.0	100.0	90.0	99.2
25-29	93.4	99.4	99.9	100.0	81.4	96.7
30-34	85.9	98.2	99.2	100.0	72.2	93.6
35-39	76.0	92.6	97.5	100.0	56.7	86.0
40-44	62.9	88.9	95.4	100.0	43.3	74.8
45-49	44.2	80.4	88.8	99.5	25.6	61.1
50-54	37.2	73.7	85.2	98.1	16.1	50.9
55-59	17.6	55.8	73.9	96.7	6.0	32.9
60-64	13.4	37.7	59.0	91.0	3.3	20.7
65-69	7.9	32.2	43.4	85.8	3.3	18.0
70-74	4.3	27.0	39.7	79.3	2.4	16.0
75-79	0.9	10.1	25.0	68.2	0.5	6.0
80-84	0.0	6.4	16.1	54.9	0.0	0.8
85-89	0.0	6.4	9.9	39.0	0.0	0.0
90-94	0.0	1.5	7.3	34.9	0.0	0.0
95-100	0.0	0.0	0.0	15.5	0.0	0.0

Malangizo Olondoledwa Pomasulira Zionetsero za Khadi la Ciwerengero

Nusu zonedwa kale munsimu zacokera:

Central Statistical Office. (2009) “Enumerator’s Instruction Manual: Living Conditions Monitoring Survey VI—2010”, catalog.ihnsn.org/index.php/catalog/2597/download/38844, zoturutsidwa 15 Juni 2017. [*Buku Lomasulira*]

Conde phunzitsani okhao ocititsa ciwerengero ndipo khazikitsani malamulo kucokera pa “Malangizo” awa

Pakabwera vuto lina lomwe silinachulidwe apa, zonse zikhale m’manja mwa wofunsayo pa gawo ili, popeza zomwezo zioneka kuti ndizo bungwe la CSO mu Zambia linacita mu 2015 LCMS. Bungwe liri lonse logwiritsa nchito khadi lapafupi la ciwerengero ca umphawi siliyenera kufalitsa matanthauzo kapena malamulo (koposa awa amene ali mu “Malangizo” ano) amene ayenera kugwiritsidwa nchito ndi anyanchito wonse woyanganira m’gawolo. Cina cili conse cimene sicinanenedwe mu “Malangizo” awa ciyenera kukhala m’manja mwa wogwira nchito imeneyi yotenga ciwerengero. Kuteroko ndimu m’mene anacitira mu 2015 LCMS.

Malangizo olondoledwa pofunsa mafunso amu khadi la ciwerengero

Conde muwerenge moloweza “Malangizo” awa ndipo munyamule pomwe mugwira nchito yanu iyi.

Pa mafunso amenewa, coyamba ngati munthu wotenga ciwerengero, lembani zoyambilira m’khadi la ciwerengero mu mutu wake komanso mu “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito”, potsata zofunikira zomwe ziri pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito”

Musafunse molunjika coonetsera coyamba ca pa khadi la ciwerengero (“Kodi pa nyumba pali anthu angati?”). M’malo mwake, gwiritsani nchito uthenga womwe walembedwa pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito” kuona pa yankho loyenera ku chonga. Muyeneranso kulemba nambala ya mamembala opezeka m’nyumbamo pa mutu wa khadi la ciwerengero pafupi ndi “Nambala ya onse okhala m’nyumba:”.

Momwemonso, musafunse molunjika coonetsera caciwiri ca pa khadi la ciwerengero (“Kodi anthu onse okhala pa nyumbapo a zaka 7 mpaka 16 amapita ku sukulu?”). M’malo mwake, gwiritsani nchito uthenga womwe walembedwa pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito” kuona pa yankho loyenera ku chonga. Makamaka, ngati “Ai” ndi *yozunguluridwa* pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito”, ndiko kuti muchonge yankho ya “A. Ai” pa coonetsera caciwiri. Ngati “Siali 7 mpaka 16” ndi yozunguluridwa pa *onse* mamembala okhala m’nyumbamo, pamenepo muchonge “C. Palibe wa 7 mpaka 16”. Mwina mwake, chongani “B. Inde”.

Musawerenge mayankho enawo kwa woyankha. Werengani cabe funso, ndipo mukatero mulekeze; ndi kuyembekezera yankho. Ngati woyankha afuna kuti mumasulire kapena azengereza kapena aoneka kuti wasokonezeka, pamenepo muwerengenso funso kapena perekani thandizo mosamalira “Malangizo” awa kapena inu, ngati wogwira nchito yaciwerengero ici, citani moyenera.

Muwerenge mafunso ndi mau omveka bwino ndithu ndipo monga m’mene yalembedwera (pokhapo ngati mwauzidwa kucitira mwina mu “Malangizo” awa) komanso monga mwa mndandanda m’mene uliri pa khadi la ciwerengero.

Monga mwa pa tsamba 73 la *Buku Lomasulira* za izi, muyenera kuyesetsa kuona (koposa kungofunsa cabe za) coonetsera ca cinai ca khadi la ciwerengero (“Kodi pansi pa nyumba pali bwanji?”) komanso coonetsera ca cisanu ca khadi la ciwerengero (“Kodi denga (mtenje) la nyumba linamangidwa ndi ciani?”). Muyenera “kukhala maso ndi kuonetsetsa ndipo inuyo muchonge mayankho ngati mutha kudziwa bwinobwino za momwe pansi pa nyumba pa liri [pansi]. Ngati simungathe kudziwa bwinobwino, muyenera kufunsa woyankhayo.” Muyenera kufunsa woyankhayo mafunso onse asanu ndi atatu (8) apa khadi la ciwerengero (mocotsako cabe mayankho a zoonetsera ziwiri zomwe mayankho ace aima pa mfundo zolembedwa pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito”).

Mukachonga yankho ya coonetsera pa khadi la ciwerengero, mulembe muzungulira yankho limenelo komanso lembani mapointszi ake, ndiponso muyalembe munsu mwa mutu wochedwa “Score” monga mwa citsanzo ici:

2. Kodi anthu onse okhala pa nyumbapo a zaka 7 mpaka 16 amapita ku sukulu?	A. Ai	0	
	B. Inde	3	3
	C. Palibe a 7 mpaka 16	6	

Monga mwa zonse, muyenera kulandira mayankho onse wopatsidwa ndi woyankhayo. Komanso, ngati woyankhayo walankhula zina zake—kapena mukuona kena kace—koonetsa kuti woyankhayo mwina akuphonya, mwina woyankhayo akukaikira, kapenanso kuti woyankhayo akufuna thandizo m'mene angayankhire, pamenepo muyenera kuwerenganso funso ndipo perekani cithandizo coyenera monga mwa “Malangizo” awa.

Pamene zoonetsera zambiri mu khadi lapafupi la ciwerengero ndi zotsimikizika kuti ndi zolungama, nthawi zambiri simuyenera kutsimikiza mayankho. Muyenera kutsimikiza yankho pokhapo ngati kena kaonetsa kuti kaphonyeka ndipo kutsimikizira pamenepo kutha kuthandiza kutenga mfundo zabwino.

Mwa citsanzo, mutha kusankha kutsimikiza ngati woyankha azangereza, aoneka ali ndi mantha, kapena mwina mwake apereka zizindikiro zoonetsa kuti iyeyo akunama kapena kuti wasokonezeka. Momwemonso, kutsimikizira ndikofunikira ngati mwana m'nyumbamo kapena mnansi anena kanthu kamene sikagwirizana ndi yankho ya woyankhayo.

Kutsimikiza kukhalanso bwino ngati inuyo mwaona kena kace—monga zinthu zimene ndizofunikira pa moyo koma sizimagulidwa kwa nthawi zonse zimene woyankhayo alinazo kapena alibe—kapena mwana alinkudya m'cipinda amene sanawerengeredwe kukhala membala wa m'nyumbamo—zimenezo zitha kuonetsa kuti yankho siili bwino ai.

Mu zambiri, zotuluka mu Khadi Lapafupi la Ciwerengero ca Umphawi liyenera kufanana kwenikweni ndi zotulukamo za 2015 LCMS la CSO mu Zambia. Mwacitsanzo, mafunso okhala ndi mapoints ayenera kucitidwa pamalo a woyankhawo cifukwa cakuti 2015 LCMS linacitidwa pamalo pa woyankhawo.

Kutembenuza Pepala la Mafunso

“Malangizo” awa—ndi chikalata ici—tsopano zipezekanso mu Chingerezi, mu Chibemba, ndi mu Chinyanja. Pakadali pano, pakalibe kukhala kutsimikizika kwa tsimitsimi kwa kutembenuza kwa khadi la ciwerengero, “Peppala la Kumbuyo Wogwiritsa Nchito”, ma tebulo auonapo a umphawi, komanso “Malangizo”awa kukhala m'zilankhulo zina zambiri zolankhulidwa ndi anthu ambiri mu Zambia monga Chitonga kapena Chilunda. Conde onani SimplePovertyScorecard.com kuti muone ngati pamenepo palinso zilankhulo zina zomwe zalembedwa kucokera pomwe izi zinalembedwa.

Ngati pakalibe kukhala kutsimikizika kwa tsimitsimi kwa kutembenuza chikalata ici mu cilankhulo cina, olankhulawo ayenera kulumikizana ndi wolembe kuti athandize kutembenuza ndi kulemba.

Malangizo ena Owonjezera

Khalidwe la Ocititsa Ciwerengero:

Monga mwa pa tsamba 4 la *Buku Lomasulira*, “Monga munthu wotenga ciwerengero, khalani aulemu komanso yesetsani kupanga ubale wabwino ndi anthu onse amene mukugwira nchito imeneyi pakati pao, kuikaponso ndi atsogoleri a m’dera limenelo limene mukugwirako nchito. Muyenera kuikako cidwi ku kafukufuku uyu pamene mukulankhula ndi anthu kuti anthu amasuke ndi kukupatseni mfundo zabwino.

“Musatsutsane ndi woyankha, kuwadzudzula (kuwathira mphepo), kapena kulankhula nao za ndale. Ngati woyankha afuna kukupititsani pambali pa nchito yanu m’makambidwe, conde pewani zimenezi mwaulemu ndithu. Ngati woyankha ndi wokwiya kapena sakugwirizana nanu, pamenepo lankhulani ndi mkulu wokuyanganirani amene adzacita zothekera zonse kuona kuti pakhale m’gwirizano.

“Muyenera kubvala bwino pamene mucita nchito imeneyi yotenga mfundo m’manyumba. Nthawi zonse khala a ukhondo ndipo bvalani movomerezeka ndi anthu a m’dera limenelo m’mene inu mukugwira nchito imeneyi.”

Cinsinsi:

Monga mwa pa tsamba 5 la *Buku Lomasulira*, simuyenera “kuonetsa, kupatsa, kukamba, kapena kuulula kwa wina aliyense wosakhala wocititsa kafukufuku aka, ngakhale kwa abale apa banja kapena kwa bwenzi mfundo ina iriyonse imene mwalandira kucokera kwa woyankha. . . . Musaye mapepala a mafunso amene mwapatsidwa poyera pamene anthu akhoza kuona zili pamenepo. Inu pokhala wotenga ciwerengero, onetetsani kuti musamalitsa ndi kusunga cinsinsi ca mapepala a mafunso ndi mfundo zimene mwalandira powasunga pamalo otetezeka nthawi zonse.”

Kuzidziwitsa kwa anthu a m’dera:

Monga mwa pa tsamba 7 la *Buku Lomasulira* za izi, m’gwirizano komanso kufuna kwabwino kwa anthu a m’dera limene mukugwiramo nchito ndikofunikira kwambiri kuti nchito imeneyi ikhale yopambana. Comweco muyenera kudziwitsa inu nokha kwa mafumu ndi atsogoleri ena odziwika bwino m’deralo kupempha m’gwirizano wao.

“Musanafunse apa nyumbapo, mwaulemu ndithu mudziwitsa nokha kuti ndinu ndani ndipo muwadziwitse cimene mwabwelera. Mukatha kufunsa, yamikani woyakhawo.”

Woyenera kuyankha:

Woyankha asakhale munthu m’modzi ngati iye akutengako mbali yofunsa pa kafukufuku uyu.

Monga mwa pa tsamba 8 la *Buku Lomasulira* za izi, “Munthu woyenera kwenikweni kuyankha ndi mutu wa nyumbayo. Ndipo watsatapo ndi mkazi wa mutu wa nyumba. Ngati awa awiriwa palibe, pezani wina aliyense amene akhoza kuyankha bwino koma wokhala panyumbapo. [Munthuyo ayenera] kukhala woyankha weniweni. Nthawi zina, mutu wa nyumba atha kukhalapo koma adzakuuzani kuti m’ malo molankhula ndi iye, mulankhule ndi wina, winayo ndiye adzakhala woyankha wanu weniweni.”

Mutu wa nyumba:

Monga mwa pa tsamba 15 ndi pa tsamba 31–32 la *Buku Lomasulira*, mutu wa panyumba ndiye “munthu amene mamembala ena onse pa nyumbapo amulemekeza ndi kumzindikira kuti ndiye mutu. Iyeyo ndiye amapanga mfundo za kayendetsedwe ka zinthu pa nyumbapo tsiku ndi tsiku. Nthawi zambiri (koma osati nthawi zonse), ameneyu ndiye mwamuna wochedwa bambo/tate m’nyumbamo. Nyumba zoti munthu akhalapo yekha, ameneyo ndiye mutu wa nyumbayo. Mutu wa nyumba akhoza kukhala wa mwamuna kapena wa mkazi.

“Munthu woyankha sindiko kuti ameneyo ndiye mutu wa nyumba. Mu manyumba ambiri amene mudzayendera, mutu wa nyumba ndiye adzakhalanso woyankha, ndiko kuti, iye amene adzapereka mfundo zambiri. Koma aliyense membala wa pa nyumbapo amene ndi wozindikira akhoza kukhala woyankha. Woyankha amene siali mutu wa nyumbayo atha kuyankha mafunso m’ malo mwa mutu wa nyumba ngati mutu wa nyumba salipo pa nthawi yoyankha mafunso.

“Kumbukirani, munthu satha kukhala mutu wa nyumba cifukwa coti iye ndiye akuyankha mafunso awa.

“Tengani munthu wamkulu pa onse kukhala ngati mutu ngati mamembala pa nyumbapo alephera kusankha wina kukhala mutu.”

Kuyamba kufunsa

Monga mwa pa tsamba 8–9 la *Buku Lomasulira*, “Kupambana kwa kufunsa kudalira pa zinthu zambiri, [zina za izo zimacitika] musanayambe kufunsa. Motero ndicofunikira kwambiri kwa inu ngati ocitisa ciwerengero kumvetsa zina mwa zinthu izi kuti pakhale kuculuka kwa otengako mbali mu kafukufuku aka. . . .

“Nthawi zonse kumbukirani kuti nthawi ya woyankhayo ndi cinthu cofunikira kwa iyeyo, ndikutinso ena (kapena ayembekezeka ku) kugwira nchito pamodzi, ndi anthu ena amene nchito zao zimagwirizana ndi maphunziro ena, motero mwina iwo sangathe kukumasukirani kweni kweni kuti apereke mfundo zokhuzana ndi m’nyumba mwao, pokhapo atsimikizadi kuti mfundo zimenezo zidzasungidwa mwa cinsinsi

kwambili. Izi zitanthauza kuti inu muyenera kubvala bwino ndi kucita zinthu mwa ubwino kwambiri ndi kuyamikira pa nthawi yomwe woyankha wakupatsani kuti mufunse mafunso anu onse.

“Coyamba cimene woyankhayo adzafuna kudziwa ndi kuti inu ndinu ndani komanso kuti mukufuna ciani. . . . Muyembekezeka kuti paciyanbi pa zonse muyenera kudziwitsa nokha pochula dzina lanu ndi kunena cilingo cimene mwafikira.

“Mwina mau anu oyamba akhoza kukhala motere: ‘Mwauka bwanji? Dzina langa ndine [dzina] ndipo ndacokera ku [dzina la bungwe]. Ndili pano kufuna kuthandiza [bungwe lathu kuti lidziwe za umoyo wa m’mene wotengako mbali ace amakhaira].’

“Woyankha ena adzafuna citsimikizo kuti mayankho ao sadzafalitsidwa kwa anthu ena mosayenera (kwa wina aliyense amene siwokhuzidwa ndi kafukufuku aka). Pamenepo muyenera kunena molimbika ndi mosaphonya mau—ndipo mutanena za kufunikira kwa woyankhayo kutengako mbali—kuti [bungwe lanu] laika malamulo okhwima kwambiri pakusunga cinsinsi ca mayankho ndi zokambirana zonse. Sizothekera kuti munthu wina wacitatu akhoza kudziwa komwe yankho lina liri lonse lacokera.

“Ngakhale mutacita zothekera zonse, pazapezekabe ena anthu amene sadzafuna konse kuti afunsiidwe ndipo akaniratu kwa mutu wa galu. Koma kumbukirani kuti, nthawi zina, kukana kotere kukhoza kukhala kuti iwo akufuna citsimikizo ceniceni. Kutu mudziwe izi padzafunika kucita ndithu mwa nzeru ku mbali yanu. Ndipo ngati woyankhayo sakufunabe kutengako mbali ndithu, pamenepo mwa ulemu wanu lailani kopanda kumuopseza.”

Mofunsira Mafunso:

Monga mwa pa tsamba 9–10 la *Buku Lomasulira*, “Muyenera kusacita tsankho ndi anthu woyankha. Samalirani kuti mau anu kapena m’citidwe wanu siuonetsa sankho, kudabwa, kubvomekeza kapena kusabvomekeza kwa mwina mafunso ofunsiidwa kapena mayankho opatsidwa. Onani kuti woyankhayo ndi inu mukhala phe musanayambe kulankhulana. Mukamafunsa mafunso, mayankho a woyankhayo afunika kutengedwa mosavuta konse ai. Inu musagwepo pamenepo ponenapo kanthu kapena ponena maganizo lanu. Mafunso amenewa alembedwa bwino moti ali pakati n’pakati; sipaganiziridwa kuti yankho lina limodzi likhoza kukhala lopambana kuposa ena onse. Ngati woyankha wapereka yankho yomwe ndi yasamvetsetseka bwino, musazitenge kuti mukudziwa zonse zimene woyankhayo akunena makamaka akamadula mau, inu musatsilize mauwo, cifukwa kawirikawiri woyankhayo adzagwirizana ndi mau anu ngakhale sanafune kunena tero, ngakhale kuti inuyo mukhoza kuphonya, iye adzagwirizana nanu.

“Mufunse mafunso monga mwa mndandanda wace; musasinthe kufunsa cifunsefunse. Mafunso amenewa alongolana mwa nzeru. Kungosintha pang’ono ndiko kuti mwaononga zinthu pa pepala limeneli la mafunso. Kufunsa mosintha mndandanda wace kutha kuonongesa mayankho olandiridwa.

“Mufunse mafunso monga momwe yalembedwera; musawasinthe ai. Ngati woyankha aonetsa kusamvetsa funso, mufunsenso mobwereza funsolo. Kuti mfundo za kafukufuku uyu [zikhale zosasinthika-sinthika], funso lina liri lonse lifunsidwe ndendende kwa woyankha wina aliyense, musasinthe kafunsidwe. Nthawi zina, woyankha satha kumvetsa funso. Ngati ndicoonekeratu kuti woyankhayo sakumvetsa funso ngakhale mutafunsanso pamenepo mutha kufunsa mwa njira ina yomveka bwino kapena kumasulira tanthauzo lace. Koma samalani kuti musakhotetse colinga ca funso limenelo.

“Musaonetse mafunso kwa woyankha. Woyankha akhoza kukopedwa podziwiratu za mafunso otsatira amene mudzamufunsa kapena akaona gawo la mayankho (amene safunsidwa pamodzi ndi mafunso).”

Malangizo akuya okhuzana ndi zina zoonetsera za m'khadi la ciwerengero

1. Kodi pa nyumba pali anthu angati?
 - A. Eyiti kapena ambiri
 - B. Seveni
 - C. Sikisi
 - D. Faifi
 - E. Folo
 - F. Filii
 - G. M'modzi kapena awiri

Musafunse funso iyi molunjika. Koma m'malo mwace, gwiritsani nchito mfundo zolembedwa pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito” kuona pa yankho limene mudzachonga. Komanso onetsetsani kuti mwalemba nambala ya mamembala a pa nyumbapo mu mutu wa khadi la ciwerengero pafupi ndi “Nambala ya onse okhala m'nyumba:”.

Monga mwa pa tsamba 14 ndi pa tsamba 29 la *Buku Lomasulira*, “pa nyumba ndi gulu la anthu lomwe nthawi zambiri amaphika, kudya, ndi kukhala pamodzi. Anthu awa akhoza kukhala abale a banja limodzi, koma amadyera pamodzi kapenanso kuika pamodzi zina zofunikira pa kukhala kwao, ndipo ali ndi munthu m'modzi amene aulemekeza kuti ndiye mutu wa nyumba. Anthu awa onse amachulidwa kuti ndi *mamembala a pa nyumbapo*.”

“Pa *nyumba* tionjezako anthu anchito ndi ena pa famu amene kawirikawiri amakhala ndi kudya pamodzi ndi mamembala apa nyumbapo. Palinso nthawi zina pamene anthu amadya pamodzi ngakhalenso kugona m'nyumba imodzi, koma ali ndi anthu ena osiyana amene amawalemekeza kuti ndiwo mutu. Anthu amenewa ayenera kutengedwa kuti ndi a m'nyumba zosiyana. Palinso nyumba zina za munthu m'modzi amene amazikonzera zakudya zace ndi zofunikira zina za mu umoyo. Munthu ameneyo akhala mutu wa nyumba.

Monga mwa pa tsamba 15 la *Buku Lomasulira*, “Ngati awiri kapena ambiri anthu/mabanja agawana nyumba—monga kugawana nyumba imodzi kapena kukhala m'zipinda za nyumba imodzi kapenanso kukhala kumalo monga m'kalasi—ndipo ngati anthuwo/mabanjawo amaika ndalama zao pamodzi ndi kugula zakudya ndi/kapenanso zinthu zina, ndiko kuti amenewa ayenera kuyesedwa ngati nyumba imodzi. Koma ngati iwo sagawana zakudya, pamenepo ayenera kuwerengedwa ngati nyumba zambiri.

Monga mwa pa tsamba 15 ndi pa tsamba 31 la *Buku Lomasulira*, pa nyumba za mitala ziyenera kutengedwa monga mwa zitsanzo izi ziwiri:

“Mwamuna wokwatira akazi ambiri, ndipo yense wa iwo akhala ndi ana ake m’nyumba yake kapena m’nyumba zingapo. Ayenera kutengedwa ngati nyumba zosiyana ngati mkazi wina aliyense wa iwo amaphika ndi kudyera payekha. Pamenepa, ngakhale kuti akaziwa nthawi zina amadyera pamodzi koma ndi cacidziwikire kuti aliyense akutsogolera nyumba yace. Motero, muwatenge iwo ngati nyumba zosiyana. Mwamuna wao mumulembe kukhala mutu kwa mkazi m’modzi cabe (mkazi wamkulu pa onse).”

“Mwamuna wokwatira akazi ambiri, amene yense wa iwo akhala ndi ana ake m’nyumba yake kapena m’nyumba zingapo. Ayenera kutengedwa ngati nyumba imodzi ngati akaziwa amaphikira ndi kudyera pamodzi.”

Monga mwa pa tsamba 16–17 ndi pa tsamba 32 la *Buku Lomasulira*, “*Membala wa nthawi zonse m’nyumbamo* ndi iye amene wakhala akukhala pa nyumbapo kwa miyezi yosacepekera pa isanu ndi umodzi (6). Iye akhoza kukhala kapena satha kukhala m’bale wa mamembala ena m’nyumbamo wa bere limodzi kapena ukwati, komanso iye akhoza kukhala wothandiza kapena wogwira nchito. *Membala wa nthawi zonse m’nyumbamo* kawirikawiri amakhala pamodzi ndi mamembala ena a m’nyumbamo m’nyumba imodzi kapena pamalo oyandikana nao ndipo amadya kucokera mu kicheni limodzi.

“Anthu amene angokwatirana kumene ayenera kutengedwa ngati *mamembala a nthawi zonse* m’nyumbamo ngakhale kuti wina wa iwo kapena onse awiri akhala m’nyumbamo kwa miyezi yocepekera pa isanu ndi umodzi.

“Ana amakanda amene abadwa kucokera kwa m’modzi wa membala wa nthawi zonse ayenera kukhala ngati mamembala a nthawi zonse m’nyumbamo.

“Mamembala a m’nyumbamo amene ali ku masukulu ogona komweko, makoleji, ndi ma yunivesite mu Zambia—kapena munthu wina amene watalikira pa nyumbapo kwa kanthawi kocepa cabe, amene nthawi zambiri amakhala ndi kudyera pomwepo (monga anthu amene anacokapa cifukwa ca nchito, kapena akudwala, anapita kumaliro, akuyembekezera kuti abereka ku malo oyembekezera, kapena anapita ukaona abale kapena abwenzi)—ayenera kuonjezedwa pa mndandanda wa mamembala a pa nyumbapo. Anthu ena ali onse amene akhala kosacepekera pa miyezi isanu ndi umodzi (6) panyumbapo naonso ayenera kuonjezedwa pa mndandanda wa mamembala a pa nyumbapo. Anthu ena onse monga ogwira nchito zapakhomo kapena m’nyumba kapena akapolo ndi anthu ena okhala nao amene ali ndithu mbali ya nyumbayo ayenera kutengedwa ngati *mamembala a nthawi zonse*.

“Mamembala a m’nyumbamo amene akhala akukhala kwina kopitilira pa miyezi isanu ndi umodzi (6) (mwa citsanzo, wina amene ali kunja kwa dziko ku maphunziro kwa miyezi yopitilira pa isanu ndi umodzi) *sayenera* kulembedwa ngati mamembala a m’nyumbamo.

“Muyenera kutsimikiza kuti mwalembe mutu wa m’nyumbayo, zaka, komanso ana amakanda. Awa amakonda kuwasiya nthawi zambiri.”

Monga mwa pa tsamba 37 la *Buku Lomasulira*, “Onetsetsani kuti mulemba okhao mamembala a m’nyumbamo. Musalembe ana a mutu omwe sakhala pa nyumbapo. Makamaka anthu acikulire kwambiri amakonda kuwerengera ana ao amenenso ali ndi nyumba zao kukhala ngati ndi a m’nyumba yao cifukwa ndi ana ao. Koma zotere sizikhuzana ndi kafukufuku ameneyu ai.”

2. Kodi anthu onse okhala pa nyumbapo a zaka 7 mpaka 16 amapita ku sukulu?
- A. Ai
 - B. Inde
 - C. Palibe a 7 mpaka 16

Musafunse funso iyi molunjika. Koma m'malo mwace, gwiritsani nchito mfundo zolembedwa pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito” kuona pa yankho limene mudzachonga. Ngati m'nyumbamo mulibe wa zaka zapakati pa 7 ndi 16, muchonge “C. Palibe a 7 mpaka 16.” Ngati m'nyumbamo muli wa zaka zapakati pa 7 mpaka 16 ndipo ngati tsopano sapita ku sukulu, pamenepo muchonge “A. Ai”. Mwina mwake, muchonge “B. Inde”.

Monga mwa pa tsamba 43–44 la *Buku Lomasulira*, “Muyenera kusamala pamene mufunsa funso ili kwa anthu amene aonekeratu kuti sapita ku sukulu.

“*Upita ku sukulu* pano titanthauza kuti munthuyo amapita ku sukulu nthawi zonse, kapena pa nthawi zina zoikika ngati wophunzira kunena kuti, munthuyo ali pa maphunziro odziwika ndiponso obvomerezeka bwino ndithu tikamanena za kuphunzira. Mwa citsanzo, onse awa atengedwa kuti akupita ku sukulu:

- Ophunzira omwe ali kumaphunziro a zaukacenjede ndi za luso (kuikapo iwo ali kumaphunziro ya zauphunzitsi)
- Ophunzira aku makoleji ndi mayunivesiti
- Anthu ophunzira sukulu usiku
- Ophunzira/ana a sukulu aku pulayimare ndi ku sekondare
- Anthu omwe ali pa chuti cosalipiridwa ca maphunziro kapena chuti cosalipiridwa amene ali m'masukulu obvomerezeka ndiponso odziwika bwino
- Anthu amene akucita maphunziro a makalata otumiza ndi masukulu omwe amacita kutumiza maphunziro yao.”

Samalirani kuti funso ifunsa za *mamembala a m'nyumbamo* ndi kuti membala wa m'nyumbamo akhoza kukhala wa mwamuna kapena wa mkazi. Ndiye, funso ikufunsa za opita ku sukulu osati anyamata okha ai koma onse anyamata ndi atsikana.

3. Kodi ndi m'giredi bwanji m'mene mkazi (wamkulu) mutu (wotsogolera)/amwao anapelera sukulu?
- A. Palibe ngakhale woyamba kufika mu giredi 1 ngakhale mu giredi 5
 - B. Giredi 6
 - C. Giredi 7 mpaka Giredi 9
 - D. Palibe mkazi wotsogolera/amwao
 - E. Giredi 10 ndi kupita pamwamba

Kumbukirani kuti mudziwa kale dzina la wamkazi wamukulu wokhalanso mutu/amwao (ndi kuti ngati alipo) kucokera ku zolembe zomwe munazilemba pa “Pepala la Kumbuyo Logwiritsa Nchito”. Motero, ngati pali mkazi amene ali mutu/amwao, musafunse kuti, “Kodi mkazi wamkulu analekezera mu giredi ciani sukulu?” Koma mufunse motere, mugwiritse nchito dzina lace la mkazi wamkulu wokhalanso mutu/amwao, mwa citsanzo: “Kodi Betty analekezera mu giredi ciani sukulu?”

Ngati palibe wamkazi amene ali mutu/amwao, pamenepo musawerenge funso ai; mungochonga “D. Palibe mkazi wotsogolera/amwao” ndipo mupite pa funso lotsatirapo.

Mwa zolinga za Khadi Lapafupi la Ciwerengero ca Umphawi, mkazi (wamkulu) mutu/amwao litanthauziridwa motere:

- Mutu wa panyumbapo, ngati wotsogolera ndi mkazi
- Wotsogolera wamkulu amwao/cibwenzi ca ukwati m'nyumbamo, ngati mutu ndi mwamuna
- Pamene palibe, ngati mutu ndi mwamuna ndipo alibe wamkazi/cibwenzi ca ukwati amene ali membala pa nyumbapo pamene mukufunsa mafunso

Monga mwa pa tsamba 15 ndi pa tsamba 31–32 la *Buku Lomasulira*, mutu wa panyumba ndiye “munthu amene mamembala ena onse pa nyumbapo amulemekeza ndi kumzindikira kuti ndiye mutu. Iyeyo ndiye amapanga mfundo za kayendetsedwe ka zinthu pa nyumbapo tsiku ndi tsiku. Nthawi zambiri (koma osati nthawi zonse), ameneyu ndiye mwamuna wochedwa bambo/tate m'nyumbamo. Nyumba zoti munthu akhalapo yekha, ameneyo ndiye mutu wa nyumbayo. Mutu wa nyumba akhoza kukhala wa mwamuna kapena wa mkazi.

“Samalirani kuti munthu woyankha sindiko kuti ameneyo ndiye mutu wa nyumba. Mu manyumba ambiri amene mudzayendera, mutu wa nyumba ndiye adzakhalanso woyankha, ndiko kuti, iye amene adzapereka mfundo zambiri. Koma aliyense membala wa pa nyumbapo amene ndi wozindikira akhoza kukhala woyankha. Woyankha amene siali mutu wa nyumbayo atha kuyankha mafunso m'malo mwa mutu wa nyumba ngati mutu wa nyumba salipo pa nthawi yoyankha mafunso.

“Kumbukirani, munthu satha kukhala mutu wa nyumba cifukwa coti iye ndiye akuyankha mafunso awa.

“Tengani munthu wamkulu pa onse kukhala mutu wa pa nyumbapo ngati mamembala alephera kusankha wina kukhala mutu.”

Monga mwa pa tsamba 15 ndi pa tsamba 45–46 la *Buku Lomasulira*, “Pamene anapelela maphunziro ndi pepala limene anatenga (mwa citsanzo, digiri, dipoloma, satifiketi, ndi zina zotero) zimene munthuyo anapata mwa njira ina iriyonse ya maphunziro; maphunziro a nthawi zonse, maphunziro a pakanthawi, kapena maphunziro ena ali onse, m’dzikoli kapena kunja kwa dziko lino, komanso opatsidwa maukulu a za maphunziro, kapena zigawo zapadera zopereka mayeso, kapena zigawo za maphunziro a za luso ndi zinchito.

“Kayendetsedwe ka sukulu kodziwika kuti masitandadi, magiredi, ndi mafomu [mu Zambia] kanasinthidwa kokwanira ngati nthawi zitatu zonse. Muyenera kusintha zakumboyo zonse za maphunziro ku nthawi zatsopano pogwiritsa nchito tebulo liri munsimu. Kwa anthu amene anapata maphunziro ao kunja kwa dziko, muyesetse ndithu kuwapatsa maphunziro olingana ndi a m’dziko la Zambia.

Kumbuyo kwa 1956	1956 mpaka 1965	1966 mpaka 1980	1981 kufikira lero
Sabu-sitandadi A	Sabu-sitandadi	Giredi 1	Giredi 1
Sabu-sitandadi B	Sabu-sitandadi	Giredi 1	Giredi 1
Sitandadi 1	Sitandadi 1	Giredi 2	Giredi 2
Sitandadi 2	Sitandadi 2	Giredi 3	Giredi 3
Sitandadi 3	Sitandadi 3	Giredi 4	Giredi 4
Sitandadi 4	Sitandadi 4	Giredi 5	Giredi 5
Sitandadi 5	Sitandadi 5	Giredi 6	Giredi 6
Sitandadi 6	Sitandadi 5 yapansi	Giredi 6	Giredi 6
Sitandadi 6	Sitandadi 6 yapamwamba	Giredi 7	Giredi 7
Fomu 1	Fomu 1	Fomu 1	Giredi 8
Fomu 2	Fomu 2	Fomu 2	Giredi 9
Fomu 3	Fomu 3	Fomu 3	Giredi 10
Fomu 4			Giredi 11
Fomu 4 (GCE)	Fomu 4 (GCE)	Fomu 5 GCE (O)	Giredi 12 GCE (O)
Fomu 6 yapansi	Fomu 6 yapansi	Form 5 GCE (O)	Giredi 12 GCE (O)
Fomu 6 yapamwamba	Fomu 6 yapamwamba	Fomu 5 GCE (A)	Giredi 12 GCE (A)
Dipoloma/satifiketi			
Maphunziro oyamba aku yunivesiti			
Digiri ya ubachala			
Satifiketi/dipoloma yapakati pa digiri yoyamba ndi digiri ya umasitala			
Digiri ya umasitala			
Digiri yapamwamba kwambili ya udotolo kapena yopitilirapo			

Mwa citsanzo:

- “Ngati wina anaphasa standadi 5 caka ca 1965 cisanafike, muwerenge kuti ndi giredi 6
- Ngati munthu anatsiriza fomu 5 GCE (O) levo mu caka ca 1980. Mu 1981, iye anapita ku maphunziro apamwamba ku University of Zambia. Patapita zaka ziwiri, anasiya asanathe maphunziro ake. Imeneyo muiwerenge kuti ndi ‘Dipoloma/satifiketi’¹
- Ngati munthu wina anatsiriza (sanayimbe cabe) giredi 7 koma tsopano akubwerezera giredi 6, ndiko kuti giredi lapamwamba lofikira ndi giredi 7
- Ngati munthu wina akubwerezera giredi 7, ndiko kuti giredi lapamwamba lofikira ndi giredi 7
- Ngati munthu wina tsopano lino akucita giredi 7 koma sanatsirizepo giredi 7, ndiko kuti giredi lapamwamba lofikira ndi giredi 6
- Ngati munthu wina anatsiriza maphunziro a Natech, ZDA, AAT, kapena ena olingana nao, pamenepo muwerengere kuti ndi ‘Dipoloma/satifiketi’
- Ngati wina anatsiriza maphunziro a ACCA, CIMA, kapena ena olingana nao, koma alibe maphunziro ena apamwamba monga digiri ya umasitala, pamenepo muwerengere kuti ndi ‘digiri ya ubachala’”

¹ Iyi mfundo ndi mau ake zioneka siziri kugwirizana mwa nzeru.

4. Kodi pansi pa nyumbayo pali bwanji? (Ngati nkotheke onani, musafunse)
- A. Thope, mitengo cabe, kapena zina
 - B. Konkiriti cabe, kapena sementi

Monga mwa pa tsamba 73 la *Buku Lomasulira*, muyenera “kukhala maso ndi kuchonga mayankho inu nokha ngati mungathe kudziwa za zomwe anapangira pansi pa nyumba. Ngati simungathe kudziwa bwino, pamenepo funsani kwa woyankha.”

“Ngati pali nsalu za kapeti zocinga pansi ponse, kapena ngati pali zina zocinga pansi ponse, onetsetsani kuti mupeza m'mene pansipo paliri.

Monga mwa pa tsamba 74 la *Buku Lomasulira*:

- *Konkiriti cabe* ndi pansi pomwe ndi posakutidwa ndi kapeti kapena ndi cina cili conse
- *Konkiriti yokutidwa* ndi pansi pomwe ndi pokutidwa ponse ndi kapeti kapena zina ziri zonse zokutira pansi

5. Kodi denga (mtenje) la nyumba linamangidwa ndi ciani? (Ngati nkotheka onani, musafunse)
- A. Udzu/maphesi, kapena zina
 - B. Malata, kapena zina zosakhala matailosi ya asibesitazi
 - C. Konkiriti, asibesitazi, kapenamatailosi ya asibesitazi

Monga mwa pa tsamba 73 la *Buku Lomasulira*, muyenera “kukhala maso ndi kuchonga mayankho inu nokha ngati mungathe kudziwa za zomwe anapangira denga la nyumba. Ngati simungathe kudziwa bwino, pamene funsani kwa woyankha.”

Monga mwa pa tsamba 73 la *Buku Lomasulira*, linena motere za zinthu zogwiritsidwa nchito ngati denga kapena mtenje wa nyumba zimene ziri motere:

- “*Udzu/maphesi* zimene kucokera kale lomwe ndizo zimagwiritsidwa nchito pakati pa anthu ena malo ena. Zimakhala bwino zikaikidwa pa ngondya ya 35 digirizi kapena kupitilirapo ndi kukhala yothikama pakati pa masentimita a 12 kufikira 15. Kuthikama kwa zovikhira zimenezi kumakula pamene ngondya icepekera.
- *Malata* amenewa kawirikawiri amakhala okutidwa ndi citsulo, kapena akhoza kukhala. Kuli malate opepuka ndipo amabwera mu mlingo wa pakati pa mamita a 1.2 ndi 3.6. Ndipo mlingo wautali utha kuugulidwa pooda. Zitha kugwiritsidwa nchitonso pa zipupa pamene ndi posalala
- *Zina zosakhala za ma asibesitazi* ndi matailosi amene amapangidwa kucokera ku zopangira zosiyanasiyana. Zimenezi zimakhala zoceperapo pa malate. Zikapangidwa kukhala zolimba kapena zouma zimapereka citetezo cabwino kapena zimakaniza moto ndi kutentha. Zimenezi kawirikawiri zimagwiritsidwa nchito kumagirako denga m’zmomangamanga zambiri
- *Malata ya ma asibesitazi* amapangidwa ndi mwala ofewa wa mtundu wa gileyi (mbuu). Ndipo zikapangidwa kukhala zolimba kapena zouma zimapereka citetezo cabwino kapena zimakaniza moto ndi kutentha
- *Matailosi a masibesitazi* ndi matailosi omwe apangidwa ndi mwala ofewa wa mtundu wa gileyi (mbuu). Ndipo zikapangidwa kukhala zolimba kapena zouma zimapereka citetezo cabwino kapena zimakaniza moto ndi kutentha. Zimenezi kawirikawiri zimagwiritsidwa nchito kumagirako denga m’zmomangamanga zambiri”

6. Kodi kwenikweni m'magwiritsa nchito mphamvu yotani pophika panyumba pano?
- Nkhuni (zotola nokha kapena zogula), malasha a mwala, zomera/matuvi a ziweto kapena zina
 - Malasha (odzipangila kapena ogula)
 - Gasi, malaiti, sola kapena parafini

Monga mwa pa tsamba 76 la *Buku Lomasulira*, “Lembani mtundu wa gwero lenileni la mphamvu yogwiritsidwa nchito pophika pa nyumbapo. Samalirani popeza pa nyumba zina zambiri amagwiritsa nchito mphamvu yoposa pa imodzi kuphika. Muyenera kufufuza modekha ndi kutsimikiza kuti akupatsani mtundu weniweni.

Monga mwa pa tsamba 76 la *Buku Lomasulira*, *mtundu weniweni wa mphamvu* “ndiwo umagwiritsidwa nchito kawirikawiri.”

Monga mwa pa tsamba 77 la *Buku Lomasulira*, linena za mitundu ya mphamvu zophikira zimene ziri motere:

- *“Nkhuni zotoledwa:* Nkhuni zotoledwa kucokera kuthengo zosagula konse
- *Nkhuni zogulidwa:* Nkhuni zogulidwa kucokera kwa anthu ena
- *Zokhalira ku mbeu/matuvi a ziweto:* Mwa citsanzo matuvi a ng’ombe, kapena zokhalira za cimanga monga mitsononkho
- *Malasha odzipangira:* Malasha opangidwa ndi anthu apanyumbapo
- *Malasha ogulidwa:* Malasha ogulidwa kucokera kwa anthu ena
- *Malaiti:* Mtundu wa mphamvu yopatsa kuwala imene imaonekera mucilengedwa (monga mkuphulika kwa mphenzi/kaleza) kapena opangidwa ndi mphamvu ya makina a jeneleta ndipo mphamvu imeneyi imayenda.
- *Sola:* Iyi ndi mphamvu yocokera ku dzuwa imene imasandulizidwa kupatsa mphamvu ya magetsi. Pamakhala *panelo ya sola* imene imakoka mphamvu ya dzuwa ndi kuisanduliza mphamvu imeneyo
- *Mwala wa malasha:* mwala wakuda wa cilengedwe umene umagwiritsidwa nchito ngatinso mafuta, zopangidwa kucokera ku zomera zakale kwambiri zimene zinafoceredwa m’nthaka ndi kusandulika miyala yotere
- *Parafini ndi mafuta:* amene amabuka akayatsidwa ndi lawi la moto ndipo ndi mafuta otenthera, ophikira komanso oyatsirako nyali

Monga mwa pa tsamba 69 la *Buku Lomasulira*, “Ngati funso lafunsidwa ndi ya gwero lenileni/mtundu wa cinthu cina ndipo ngati panyumbapo agwiritsa nchito gwero/mtundu, pamenepo mulembe cabe mtundu womwe amagwiritsa nchito nthawi zambiri. Mu nthawi zina, mudzayenera kufufuza kuti mutsimikize bwino za gwero lenileni limeneli.”

7. Kodi m’nyumba yanu muli ndi wailesi yakanema (TV), ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi/ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV?
- A. Mulibe TV (ngakhale zina zilipo)
 - B. TV cabe, mulibe zina
 - C. TV, ndi zina (DVD, dishi ndi zina)

Coonetsera ici mucifunse mu magawo awiri:

- Kodi m’nyumba yanu muli ndi wailesi yakanema (TV)?
- Does your household own any DVDs/VCRs, home theatres, satellite dish/decoders (free to air, or DSTV), or other pay-TV arrangements?
- Kodi m’nyumba yanu muli ndi ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi, ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV?

Muchonge yankho monga mwa mafunso ofunsidwa awiriwa:

Wailesi ya Kanema (TV)	ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi/ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV?	Yankho
Ai	Ai	A
Inde	Ai	B
Ai	Inde	A
Inde	Inde	C

Monga mwa pa tsamba 67 la *Buku Lomasulira*, “*homu fiata* ndi makina opereka mau/kanema wacisangalalo wokhala ndi wailesi ya kanema yokhala ndi hi-fi yokhala ndi masipika atatu (ku la manzere, ku la manja ndi pakati) komanso ndi masipika kumbuyo ku la manzere ndi ku lamanja.

“*Satelaiti dishi/dekhoda* ndi mtundu wa cimbale cosanoka comwe cikhala mulongoti wolandira ndi kupereka zizindikiro zimene zimacokera ku satelaiti. Iwo amene ali ndi madishi a satelaiti ndi madekhoda amalipira ndalama kwa eni ake a sithoni ya TV. *TV yogwiritsa nchito satelaiti* yolipiridwa imaulutsa ndi kufalitsa ndondomeko zimene anthu atha kulipira kuti aonere wailesi ya kanema kupyolera mwa cimbale copangidwa ngati dishi cimene cimalandira zizindikiro. Iwo amene amalipira ndalama ya satelaiti TV amatha kuona TV imeneyo. Zitsanzo za iwo olipiridwa popereka maser-visi otero ndi GTV (tsopano inatsekedwa) ndi Multichoice. Dishu ya

satelaiti ndi dekhoda zitha kugwiritsidwa nchito kuona masiteshoni amene atha kuonedwa mosalipira konse makamaka aja odziwika kuti ndi aulere.”

Monga mwa pa tsamba 64–65 la *Buku Lomasulira* za izi, “Apa anena za ma wailesi yakanema (ma TV), ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi, ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV za eni nyumba ndiponso zimene zili bwino-bwino moti panopa akugwiritsidwa nchito, kapena zomwe ziliko ndi vuto pang’ono komabe zikugwiritsidwa nchito. Musawerengere pamodzi ndi zoonongekeratu zimene sizigwira nchito.

“Ngati eni nyumba akusunga wailesi yakanema (TV), DVD/VCR, cilimba ca homu fiata, satelaiti dishi, dekhoda (yopereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV ya munthu wina ndipo akuigwiritsa nchito, conde musaiwerenge ngakhale kuti aisunga kwa zaka ndithu.

“Ma wailesi yakanema (ma TV), ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi, ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV zopatsidwa ngati colowa ziyenera kuonkhetsedwa pa katundu malinga ngati zili bwino-bwino.

“Wailesi yakanema (TV), DVD/VCR, cilimba ca homu fiata, satelaiti dishi, dekhoda (yopereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV zimene ndi za anthu awiri kapena angapo, siziyenera kulembedwa kuti ndi za wakuti-wakuti ai. Koma ma wailesi yakanema (TV), ma DVD/VCR, zilimba za homu fiata, satelaiti dishi, ma dekhoda (opereka ndondomeko za ulere, kapena DSTV) kapena zina zolipilidwa pa TV zomwe ndi za m’nyumba imodzi ndi zokhazo zomwe ziyenera kulembedwa.”

8. Kodi m’nyumbamo muli ndi nsimbi yosakhala ya malaiti kapena ya malaiti?
 A. Mulibe
 B. Muli yosakhala ya malaiti cabe
 C. Ya malaiti, kapena zonse, ya malaiti ndi yosakhala ya malaiti

Coonetsera ici mucifunse mu magawo awiri:

- Kodi m’nyumbamo muli ndi nsimbi za malasha kapena zosakhala za malaiti?
- Kodi m’nyumbamo muli ndi nsimbi za malaiti?

Muchonge yankho monga mwa mafunso ofunsidwa awiriwa:

Nsimbi zosakhala za malaiti (mwina za malasha)?	Nsimbi za malaiti?	Yankho
Ai	Ai	A
Inde	Ai	B
Ai	Inde	C
Inde	Inde	C

Monga mwa pa tsamba 67 la *Buku Lomasulira*, “nsimbi yosakhala ya malaiti siigwiritsa nchito malaiti kuti itenthe. Citsanzo ca nsimbi zotere mu Zambia ndi zija zomwe zimagwiritsa nchito malasha.”

Monga mwa pa tsamba 64–65 la *Buku Lomasulira* za izi, “Apa anena za nsimbi zosakhala za malaiti kapena nsimbi za malaiti za eni nyumba ndiponso zimene zili bwino-bwino moti panopa akugwiritsidwa nchito, kapena zomwe ziliko ndi vuto pang’ono komabe zikugwiritsidwa nchito. Musawerengere pamodzi ndi zoonongekeratu zimene sizigwira nchito.

“Ngati eni nyumba akusunga nsimbi yosakhala ya malaiti kapena nsimbi ya malaiti ya munthu wina ndipo akuigwiritsa nchito, conde musaiwerenge ngakhale kuti aisunga kwa zaka ndithu.

“Nsimbi zosakhala za malaiti kapena nsimbi za malaiti zopatsidwa ngati colowa ziyenera kuonkhetsedwa pa katundu malinga ngati zili bwino-bwino.

“Nsimbi yosakhala ya malaiti kapena nsimbi ya malaiti imene ndi ya anthu awiri kapena angapo, siiyenera kulembedwa kuti ndi ya wakuti-wakuti ai. Nsimbi zosakhala za malaiti kapena nsimbi za malaiti zokhazo zimene ndi za m’nyumba imodzi ndizo ziyenera kulembedwa.”

9. Kodi pa nyumbapo muli ndi ma selefoni?
A. Ai
B. Inde

Monga mwa pa tsamba 64–65 la *Buku Lomasulira* za izi, “Apa anena za ma selefoni a eni nyumba ndiponso amene ali bwino-bwino oti panopa akugwiritsidwa nchito, kapena omwe aliko ndi vuto pang’ono komabe agwiritsidwa nchito. Musawerengere pamodzi ndi woonongekeratu amene sagwira nchito.

“Ngati eni nyumba akusunga selefoni ya munthu wina ndipo akuigwiritsa nchito, conde musaiwerenge ngakhale kuti aisunga kwa zaka ndithu.

“Maselefoni opatsidwa ngati colowa ayenera kuonkhetsedwa pa katundu malinga ngati ali bwino-bwino.

“Selefoni imene ndi ya anthu awiri kapena angapo, siyenera kulembedwa kuti ndi ya wakuti-wakuti ai. Maselefoni okhao amene ndi am’nyumba imodzi ndiwo ayenera kulembedwa.”

10. Kodi m’nyumbamo muli ndi mibedi ingati komanso mamatilesi angati?

- A. Mulibe
- B. Bedi imodzi kapena mibedi yambiri koma mulibe matilesi
- C. Matilesi imodzi (mosawerengera mibedi ndi ingati)
- D. Mamatilesi awiri kapena ambiri (mosawerengera mibedi ndi ingati)

Coonetsera ici mucifunse mu magawo awiri:

- Kodi m’nyumbamo muli ndi mibedi ingati?
- Kodi m’nyumbamo muli ndi mamatilesi angati?

Muchonge yankho monga mwa mafunso ofunsidwa awiriwa:

Nambala ya mibedi?	Nambala ya mamatilesi?	Yankho
Mulibe	Mulibe	A
M’modzi kapena ambiri	Imodzi	C
Mulibe	Awiri kapena ambiri	D
M’modzi kapena ambiri	Mulibe	B
Mulibe	Imodzi	C
M’modzi kapena ambiri	Awiri kapena ambiri	D

Monga mwa pa tsamba 64–65 la *Buku Lomasulira* za izi, “Apa anena za mibedi ndi mamatilesi a eni nyumba ndiponso amene ali bwino bwino oti panopa akugwiritsidwa nchito, kapena omwe aliko ndi vuto pang’ono komabe agwiritsidwa nchito.

Musawerengere pamodzi ndi zoonongekeratu zimene sizigwira nchito.

“Ngati eni nyumba akusunga bedi kapena matilesi ya munthu wina ndipo akuigwiritsa nchito, conde musaiwerenge ngakhale kuti aigwiritsa nchito kwa zaka ndithu.

“Mibedi kapena mamatilesi opatsidwa ngati colowa ayenera kuonkhetsedwa pa katundu malinga ngati ali bwinobwino.

“M’bedi kapena matilesi imene ndi ya anthu awiri kapena angapo, siiyenera kulembedwa kuti ndi ya wakuti-wakuti ai. Mibedi kapena mamatilesi okhao amene ndi am’nyumba imodzi ndiwo ayenera kulembedwa.”